



Fig. 5. Mopangira migwere ya desmodium

- Sakanizani desmodium ndi fateleza wa superphosphate (dzanja limodzi lodzala njere ndi manja awiri odzala fateleza).
- One kilogramme (1 kg) ya njere za desmodium ndiwo mlingo wofunikira pa eka imodzi ya nthaka.
- Ngati simukwanitsa kugula fateleza, sakanizani cabe njere za desmodium ndi doti yabwino. Byalani mu mgwere mwapanaga ndi kuundira ndi doti mwapan'ono (Fig. 5).
- Desmodium uyeneranso kuwazidwa pa mbali zonse ziwiri za mizere ya chimanga ya kunja pa m'mpata wa 37.5 cm pa mzere ndi mzere.
- Byalani desmodium pomwe kuli mvula motero kuti imere bwino.

Gawo 3 Kupalira Kupalira ndi kusamalira mbewu Mbeu

- Kupalira msanga ndi kofunikira motero kuti munda wa mkankho-kokera ukhazikitsidwe bwino.
- Palirani nthawi yoyamba pomwe chimanga ciri ndi masabata atatu ndipo mupalire kachiwiri pomwe chimanga ciri ndi masabata asanu.
- Ndikofunikira kusiyanitsa pakati pa desmodium ndi udzu (Figs 6 and 7).




Fig 6. Timbewu ta desmodium ta masabata atatu ndi ta masabata asanu




Fig 7. Kupalira ndi manja timbewu ta desmodium tobyalidwa pakati pa mbewu ya chimanga



icipe

CHINYANJA - ZAMBIA



Ngati m'kufuna kudziwa zambiri, khudzanani ndi:
A Principal Scientist,
Habitat Management Programme (icipe),
P. O. Box 30-40305, Mbita Point, Kenya,
Pa lamya 059 22216-18.
E-mail: zkhan@icipe.org

International Center of Insect Physiology and Ecology (ICIPE), Kenya with Rothamsted Research, UK, Kenya Agricultural Research Institute (KARI) and Ministry of Agriculture (MOA), Kenya

Donors:

Kilimo Trust East Africa, Biovision Switzerland and European Union

Visit website: www.push-pull.net

M'njira ya mkankho-kokera udzu wa nsenjere umabyalidwa mozungulira mbewu ya chimanga monga mbewu ya msampha. Mphutsi zodowola tsinde zimakokedwa kutali ndi chimanga. Mphutsi zodowola zimaikira mazira pa udzu wa nsenjere koma udzu siurnalola agulugufe kukhwima ai. Desmodium umabyalidwa pakati pa mizere ya chimanga. Ndipo umaturutsa kafungo komwe chifukufuku odowola tsinde samakonda motero amakankhidwa kutali ndi mbewu ya chimanga. Desmodium uthandiziranso kuika chonde m'nthaka ndi kuletsa udzu wa kaloyi kukula kapena kuziphaticiza ku midzu ya chimanga. Motero chimanga chipulumutsidwa ku mphutsi zodowola tsinde ndi udzu wa kaloyi pomwe cabyalidwa mogwirtsita ntchito njira ya mkankho-kokera..

KABYALIDWE KOGWIRITSA NTCHITO NJIRA YA MKANKHO-KOKERA

Gawo 1. Kakhondedwe ka nthaka

- Khozani nthaka yanu m'nthawi ya dzuwa.
- Chitani galauza ndi kuvara nthaka yanu kuti ikhale yofewa kwambiri mvula isanayambe.
- Desmodium uli ndi njere zazing'ono kwambiri; motero, samalani nthaka yanu pomwe mu kuikhonza kuti ikhale yofewa.
- Gawani munda wanu wa mkankho-kokera motero kuti mubyale mizere itatu ya udzu wa nsenjere mozungulira m'malire (Fig. 1).




Fig. 1. Mokhazikitsira munda pogwirtsita ntchito njira ya mkankho-kokera

Gawo 2. Kabyalidwe

Kabyalidwe ka udzu wa nsenjere

- Byalani udzu wa nsejere (Mtundu wa Bana) m'malire mozungulira munda wa chimanga.
- Byalani mizere itatu ya udzu wa nsenjere mozungulira munda wa chimanga. Mipata iyenera kuhala 75 cm pakati pa mizere ndi 75 cm pakati pa mbewu m'mzere (Fig. 2).




Fig. 2. M'pata wa udzu wa nsenjere

- Ikani tisipuni yodzala fataleza wa triple superphosphate imodzi kapena manja awiri wodzala ndi manyowa apa pulazi owolera bwino m'dzenje liri lonse musanabyale udzu wa nsenjere.
- Ikani nzimbe ya mfundo zitatu ndi kutsimikizira kuti mfundo ziwiri zaundiridwa m'nthaka kapena ikani midzu yopatulidwa m'dzenje yobyalamo ndi kuundira ndi doti (Fig. 3).




Fig. 3. Mobyalira udzu wa nsenjere

Kabyalidwe ka desmodium

- Desmodium uyenera kubyalidwa m'mizere mosinhanitsana ndi mizere ya chimanga (Ndiko kuti osati pa mzere umodzi ndi chimanga) motero kuti ulimi wa m'chaka chotsatira ukakhale wofewa (Fig. 4).

Kabyalidwe ka chimanga

- Byalani chimanga canu m'munda wozunguliridwa kale ndi udzu wa nsenjere.
- Tsimikizirani kuti mzere woyamba wa chimanga uli 1 m kutali ndi mzere wa m'kati wa udzu wa nsenjere.
- Mipata yovomerezewa ya chimanga ndi 75 cm pakati pa mizere ndi 30 cm pakati pa zitunda m'mzere.
- Ikani tisipuni imodzi yodzala triple superphosphate kapena ma tisipuni awiri odzala single superphosphate pa dzanje limodzi.




Fig. 4. Sinthanitsani mizere ya desmodium ndi mizere ya chimanga

Kubyala desmodium ndi mbewu ina

- Wazani Desmodium pakati pa mizere ya chimanga ya mipata 75 cm pa mzere ndi mzere wina.
- Gwiritsani ntchito mtengo wolimba wakuthwa kutsogoro, kupanga ka mgwere kozama 1-2 cm pakati pa mizere yobyalamo chimanga (Fig. 5).